Kulambira Kumene Mulungu Amavomereza (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 15 m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* Bukuli likupezekanso pawebusaiti ya jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI MULUNGU AMASANGALALA NDI ZIPEMBEDZO ZONSE?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani anthu ena anganene kuti inde Mulungu amasangalala nazo?

N'chifukwa chiyani ena anganene kuti ayi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Tizipembedza Mulungu m’njira imene amavomereza.

(Werengani mutu 15 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1-4.)

Werengani Mateyu 7:21-23.

Mogwirizana ndi zimene Yesu ananena, n’chifukwa chiyani si zokwanira **kungonena** kuti timakhulupirira Yesu kapena Atate wake?

_____

_____

_____

Werengani Mateyu 7:13, 14.

N’chifukwa chiyani si zodabwitsa kuti anthu ambiri sanapezebe chipembedzo choona?

_____

_____

_____



Ngati tingadziwe mmene ndalama yeniyeni imaonekera zingatithandize kudziwa mosavuta ndalama yachinyengo. Mofanana ndi zimenezi, tikadziwa chipembedzo choona, tingathenso kuzindikira mosavuta chipembedzo chonyenga.

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Anthu amene ali m’chipembedzo choona timawadziwa ndi zimene amakhulupirira komanso zimene amachita.

(Werengani mutu 15 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 5-14.)

Werengani Salimo 83:18, Mateyu 20:28, ndi 2 Timoteyo 3:16, 17.

Kodi Akhristu oona amakhulupirira zotani pa nkhani ya Mulungu, Yesu, komanso Baibulo?

Werengani Mateyu 24:14, Maliko 12:17, ndi Yohane 13:35.

Kodi Akhristu oona amachita zinthu zotani pamoyo wawo zomwe zimasonyeza kuti ali m’chipembedzo choona?

N’chiyani **chimakutsimizirani** kuti Mboni za Yehova ndi chipembedzo choona?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Zipembedzo zonse ndi zabwino.

MUNGAYANKHE KUTI…

Ndi zoona kuti m’zipembedzo zonse muli *anthu* abwino. Koma ndimakhulupirira kuti pali chipembedzo chimodzi chokha chimene Mulungu amachivomereza chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo ya palembali?

_____

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Chipembedzo chathu n’chimodzi mwa zipembedzo zazikulu kwambiri padziko lapansi ndipo muli anthu ambiri, sindikuganiza kuti anthu onsewo ndi osazindikira.

MUNGAYANKHE KUTI…

Anthu ambiri akhozanso kunena choncho. Koma ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo ya palembali?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania